zonse zabwino kwambiri.
-Ndipo Satana anakwiya kwambiri .

-Nazonso ziwanda za Satana zinawona kuti Mulungu analenga zinthu zonse zabwino kwambiri.

-Nazonso ziwanda za Satana zinakwiya kwambiri.



PHUNZIRO LA 7

1. Kodi dziko la pasi linali lotani Mulungu asanalilenge?
-Pachiyambi, kunalibe kuwala.
-Pachiyambi, mdima unali ponseponse pa dziko la pasi.

2. Kodi Mulungu analenga bwanji kuwala pa tsiku loyamba?
-Kungolankhula.

3. Kodi Mulungu analenga bwanji mlengalenga pa tsiku lachiŵiri?
-Kungolankhula.

4. Kodi Mulungu anaŵalekanitsa bwanji madzi amene anali ponseponse pa dziko la pasi?
-Mulungu anaŵayika madzi ena mu mlengalenga kuchokera pa dziko la pasi.
-Mulungu anaŵasiya madzi ena onse otsala pa dziko la pasi.

5. Kodi amene anaŵalamula madzi kuti asendere mmbuyo kuti mtunda uwoneke ndani?
-Mulungu.

6. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu yekha ndi amene angaŵalamule madzi kuti asendere mmbuyo, madziwo ndikumvera?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene analenga madzi.

7. Kodi Mulungu anadziŵa bwanji kulenga zonsezi?
-Palibe chimene Mulungu sachidziŵa.

8. Kodi kunali kovuta kwa Mulungu kuti Iye alenge zonsezi?
-Iyayi.

9. Kodi chifukwa chiyani sikunali kovuta kuti Mulungu alenge zonsezi?
-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Palibe china chilichose chimene Mulungu sangathe kuchichita.

-10. Kodi Mulungu anamulengela ndani zomera zonse ndi mitengo, somba ndi mbalame, ndi zinthu zina zonse?
-Mulungu anaŵalengera anthu zinthu zonsezi.

11. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵalengera anthu zomera zonse ndi mitengo, somba ndi mbalame, ndi zinthu zina zonse?
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu kwambiri.

12. Kodi chifukwa chiyani dzuŵa, mwezi ndi nyenyezi sizigwa kuchokera mu mlengalenga?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anazisiya kumeneko.
-Chifukwa chakuti ntchito ya Mulungu ndi yabwino kwambiri.

13. Kodi Mulungu ananena chiyani pa zinthu zonse zimene Iye analenga?
-Mulungu ananena kuti zinthu zonse zinali zabwino.

14. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anatha kulenga zinthu zonse zabwino kwambiri?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.

-Kodi Mulungu analenga chiyani pa tsiku lachisano ndi limodzi?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:24-25



- Kodi dziko la pasi ndi la ndani?
-Mulungu.

-Kodi anali maganizo a ndani olenga wina wake kukhala oyang'anira dziko la pasi?
-A Mulungu yekha.

-Mulungu anapanga dziko, ndipo anasankha anthu kukhala oyang'anira dzikolo.

-Kodi Mulungu anati chiyani atatha kulenga zinthu zonse?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:31

31-Mulungu anaziwona zonse zimene Iye anazilenga kuti zinali zabwino kwambiri. Ndipo kunada, ndiponso kunacha. Ili linali tsiku la chisano ndi limodzi.

-Mulungu atatha kulenga zinthu zonse, Iye anaziwona kuti zinali zabwino kwambiri.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri, zinthu zonse zimene amazilenga Mulungu zimakhala zabwino kwambiri.

-Pachiyambi, kunalibe minga.
-Pachiyambi, kunalibe zomera.
-Pachiyambi, nyama sizimaŵaluma anthu.
-Pachiyambi, Mulungu anazilenga zinthu zonse zabwino kwambiri.

-Angelo a Mulungu anawona kuti Mulungu analenga zinthu zonse zabwino kwambiri.
-Ndipo anali kusangalala.

-Satana nayenso anawona kuti Mulungu analenga zinthu

wakuda khungu.
-Pachiyambi Mulungu analenga munthu wamamuna mmodzi ndi wamkazi mmodzi.

-Anthu onse akuchokera kwa Adamu.
-Anthu onse ndi zidzukuru za Adamu.

-Pamene Mulungu anamulenga Adamu, Iye anamupanga Adamu kukhala mfumu ya dziko la pasi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:28

28-Mulungu anaŵadalitsa ndipo anaŵawuza kuti, "Mubereke ndi kuchulukana, mudzadze dziko lonse la pasi ndikumalilamulira . Ndakupatsani ulamuliro pa msomba za mnyanja ndi mbalame zowuluka mu mlengalenga ndi za moyo zonse zokwaŵa pa dziko la pasi."

-Mulungu anamulenga Adamu, ndipo anamupanga kukhala olamulira zonse za pa dziko la pansi.

-Mulungu sanazipange nyama kukhala zolamulira dziko la pansi.
-Mulungu sanaŵapange angelo kukhala olamulira dziko la pasi.

-Mulungu sanamupange Satana ndi ziwanda zake kukhala olamulira dziko la pasi.

-Mulungu anaŵalenga anthu kukhala olamulira dziko la pasi.

-Kodi amene analenga dziko la pasi ndani?
-Mulungu.



24-Ndipo Mulungu adati, "Pa dziko la pasi pakhale mitundu yonse ya za moyo potsata mitundu yake: zoweta, zokwaŵa, , ndi nyam za ku thengo, potsata mitundu yake." Ndipo zinachitikadi.

25-Pomwepo Mulungu adalenga nyama za ku thengo potsata mitundu yake, ndi nyama zoweta potsatanso mitundu yake, ndiponso zokwaŵa zonse patsatanso mitundu yake. Mulungu adawona kuti zonse zimene analengazo zinali zabwino.

-Pa tsiku lachisano ndi limodzi, Mulungu analenga nyama zonse.

-Kodi Mulungu analenga nyama za mitundu yingati?
-Yambiri, palibe amene angathe kuŵerenga.

-Kodi angelo anakatha kulenga nyama?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kulenga nyama.

-Kodi anthu anakatha kulenga nyama?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kulenga nyama.

-Kodi nyama zinakatha kuzilenga zokha?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi amene angathe kulenga nyama.

-Mulungu atatha kulenga nyama, dziko la pansi linatha kukomzedwa.

-Kodi Mulungu anamukonzera ndani dziko la pasi?
-Mulungu anaŵakonzera anthu dziko la pasi.

-Mulungu anaŵakonzera anthu dziko labwino kwambiri

chifukwa chakuti Iye amaŵakonda anthu kwambiri.

-Mulungu sanaŵakonzere angelo dziko la pasi.
-Mulungu sanazikonzere ziwanda dziko la pasi.
-Mulungu sanamukonzere Satana dziko la pasi.

-Mulungu anaŵakonzera anthu okha dziko la pasi.

-Tiyeni toŵerenge zimene Mulungu analakhula atatha kuŵakonzera anthu dziko la pasi.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:26

26-Kenako Mulungu anati, "Tiyeni tipange munthu mchifanizo chathu, adzakhale ngati ifeyo. Adzalamulire somba za mnyanja, mbalame za mu mlengalenga, nyama zoweta, ndi zokwaŵa zonse za pa dziko la pasi."

-Mulungu anati," Tiyeni tipange munthu mchifanizo chathu."
-Kodi Mulungu amkalamkhula kwa ndani?

-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi) ndi Mulungu Mzimu woyera amkalamkhulana.

-Mulungu Atate, Mulungu mwana (Mpulumutsi) ndi Mulungu Mzimu woyera amkalamkhulana zoŵapanga anthu mu chifanizo chawo.

-Kodi chofunika kwambiri pa zinthu zonse zimene Mulungu analenga chinali chiyani?
- Anthu.

-Chifukwa chakuti anthu ndi amene anali ofunika kwambiri pa zinthu zonse zimene Mulungu analenga, kodi Mulungu anaganiza zomulenga bwanji munthuyo?



-Kodi Adamu anakatha kudzilenga yekha?
-Iyayi.

-Kodi amene anamulenga Adamu anali ndani?
-Mulungu.

Tiyeni tiŵerenga Genesesi 2:7a

7-Ambuye Mulungu anawumba munthu ndi dothi la pansi.

-Mulungu anamulenga Adamu ndi dothi la pasi.
-Koma Adamu analibe moyo.
-Kodi chifukwa chiyani?

-Chifukwa chakuti Mulungu anali asapumulile moyo mwa Adamu.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 2:7b

7-Ambuye Mulungu anapumira mphuno mwa Adamu mphumu za moyo ndipo iye anakhala ndi moyo.

-Adamu anakhala ndi moyo Mulungu atamupumulira iye mphumu za moyo.

-Mulungu yekha ndi amene angathe kupumila moyo mwa anthu.
-Mulungu yekha ndi amene angapereke moyo.

-Adamu ndi chiyambi cha mtundu onse wa anthu.
-Adamu ndi kholo la mtundu onse wa anthu.

-Pachiyambi Mulungu sanalenge munthu wofira kapena

koti lipite?

-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti bwato silimakhala ndi chifuniro.

-Mulungu ali ndi chifuniro, ndipo Iye anaŵalenganso anthu ndi chifuniro.

-Mulungu akufuna kuti anthu adzimusankha Mulungu.
-Mulungu akufuna kuti anthu adzimusankha Iye.

-Tiyeni tiŵerenge za kulengedwa kwa munthu oyamba:

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 1:27

27-Chomcho Mulungu anamulenga munthu mchifaniziro Chake, mchifaniziro cha Mulungu anamulenga iye; anamulenga wamkazi ndi wamamuna.

-Pachiyambi, Mulungu anamulenga munthu wamamuna oyamba.
-Kenako, Mulungu anamulenga munthu wamkazi oyamba.

-Dzina la munthu wamamuna woyamba linali Adamu.
-Dzina lakuti Adamu likumasulira kuti, "Munthu."
-Kodi nyama zinatha kumulenga Adamu?
-Iyayi.

-Kodi angelo anatha kumulenga Adamu?
-Iyayi.

-Kodi Satana ndi ziwanda zake anatha kumulenga Adamu?
-Iyayi.



-Mulungu anaganiza zomulenga munthu mu chifanizo Chake.

- Kodi zikuthandawuza chiyani kuti munthu analengedwa mu chifanizo cha Mulungu?

-Sizikuthandawuza matupi athuŵa, chifukwa chakuti Mulungu alibe thupi la mnofu, mafupa ndi magazi.

-Mbali ya ife imene Mulungu anayilenga mu chifanizo Chake, siyingawoneke.

-Mbali ya ife imene Mulungu anayilenga mu chifanizo Chake ndi moyo wathu.

-Mmoyo mwathu tili ndi mbali zitatu.
-Mmoyo mwathu, tili ndi mzeru, maganizo a mphamvu, ndi chifuniro.

-Mulungu anaŵalenga maganizo athu mu chifaniziro chake.

-Chifukwa chakuti Mulungu ali ndi nzeru, Iyeyo anaŵalenga anthu ndi mzeru.
-Mulungu amaganiza, ndipo Iye akufuna kuti anthu adziganizanso.

-Mulungu amafuna kuti anthu adziganiza zinthu zabwino.

-Mulungu amafuna kuti anthu adziganiza za Mulunguyo.
-Mulungu akufuna kuti anthu adzimudziŵa Iye.

-Kodi inu mungasangalale kumakakhala ku tchile ndi nyama ndi kumakalankhulana nazo?

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti nyama siziganiza.

-Mulungu sanazilenge nyama mu chifaniziro chake.
-Mulungu sanazilenge nyama ndi mzeru.

-Mulungu akufuna kuti anthu aziyankhulana naye ngati mmene mumalankhulilana ndi amzanu.

-Mulungu ali ndi nzeru, ndipo anaŵalenga anthu ndi nzeru.

-Mulungu akufuna kuti anthu adziganiza za Mulunguyo.
-Mulungu akufuna kuti anthu adzimudziŵa Iye.

-Mulungu anaŵapanganso maganizo athu kukhala amphamvu mchifaniziro chake.

-Chifukwa chakuti Mulungu ali ndi maganizo a mphamvu kwambiri, Iye anaŵalenga anthu ndi maganizo amphamvunso.

-Mulungu amasangalala ndipo Iye amafuna kuti anthu adzikhala osangalalanso.

-Mulungu amafuna kuti anthu adzikhala osangalala ndi za Mulungu.
-Mulungu amafuna kuti anthu adzimukonda Iye.

-Mulungu amachida chinthu ndiponso amadandawula.
-Kodi Mulungu amadana ndi chiyani?
-Mulungu amadana ndi machimo onse.

-kodi tchimo ndi chiyani?
-Tchimo ndi chinthu chimene Mulungu samachifuna.
-Tchimo ndi zinthu zonse zimene Mulungu samazifuna.



-Kodi Mulungu amadandawula ndi chiyani?
-Mulungu amadandawula za anthu amene sakumukonda Iye.

-Mulungu amakukondani inu ngati mmene mumaŵakondera ana anu.

-Mulungu ali ndi maganizo amphamvu kwambiri chomcho Iye anaŵalenganso anthu ndi maganizo amphamvu kwambiri.

-Mulungu akufuna kuti anthu adzikhala osangalala ndi za Mulungu.
-Mulungu akufuna kuti anthu adzimukonda Iye.

-Mulungu analenga chifuniro chathu mchifaniziro Chake.

-Chifukwa chakuti Mulungu ali ndi chifuniro, Iye anaŵalenganso anthu ndi chifuniro.
-Mulungu amatha kusankha, ndipo Iye akufuna kuti anthu adzitha kusankhanso.

-Mulungu amafuna kuti anthu adzitha kusankha zinthu zimene zili zabwino.
-Mulungu amafuna kuti anthu adzimusankha Iye.
-Mulungu amafuna kuti anthu adzisankha kumumvera Iye.

-Kodi mukawomba mfuti, mfutiyo imasankha chinthu chimene inu mukufuna kuchiwomberacho?
-Iyayi.
-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti mfuti siyimakhala ndi chifuniro.

-Kodi mukamapalasa bwato pa madzi, bwatolo limasankha